

CHAKUYA

CHIMAYITANIRA KU CHAKUYA



Palibe Mizimu Yoyera iwiri. Ndiwo...Ndipo Woyera womwewo unamutsogolera Simioni, usiku uja, kapena mmawa uja, kwa Khristu, wakutsogolerani inu pano usikuuno, chifukwa inu mukukhulupirira lonjezo la Mzimu Woyera. Ndipo Iye ali wokakamizika basi kwa inu monga momwe Iye anali kwa Simioni, chimodzimodzi, chifukwa Iye ndi Mulungu, ndipo Iye ayenera kusunga Mawu Ake.

Ndiye ine ndikukhoza kumuwona Simioni, iye ankalakalaka, iye ankakhumba kuti amuwone Khristu. Iye anakhulupirira chimene Mawu a Mulungu anali atanena kwa iye. Zinalibe kanthu zomwe otsutsa ankanena, iye anakhulupirira Mawu a Mulungu. Panali kulirira mu mtima wake kuti amuwone Khristu, ndipo iye anakhulupirira kuti iye akanadzatero. Monga Davide anati, “Pamene chakuya chiyitanira ku Chakuya.”

Ambiri a inu mkati muno mumakhulupirira mu machiritso Auzimu. Ndi choncho inu? Kodi inu mukukhulupirira mu machiritso Auzimu? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Chifukwa chimene chomwe inu mukukhulupirira mu machiritso Auzimu, chikutsimikizira kuti alipo machiritso Auzimu.

Pamene ife tinabwera ku Amereka, ife tinawapeza Amwenye Achimereka. Iye anali akupembedza chinachake, dzuwa, mwezi, ndi chirengedwe. Chifukwa, mwa iye, iye ndi munthu wokhalapo, ndipo iye ankadziwa kuti iye ali naye womupanga, kotero panali chinachake mkati mwa mtima wake waumunthu chinkayitanira kuti azipembedza.

Izo ziri kwa wachivundi aliyense. Inu mukhoza kumapembedza galimoto yanu, ntchito yanu, nyumba yanu, kapena chinachake; inu mudzapembedza chinachake. Kotero, ngati pali fano lililonse, lichotseni ilo ndipo mumulole Yesu Khristu atenge malo oyambirira. Mumulole Iye akhale woyamba wa zonse.

Ndiye, njala, kuya. Monga Davide ananena.

Pamene kuya kuyitanira ku kuya pa phokoso la mathithi a madzi anu: . . .

Tsopano, “kuya kuyitanira ku Kuya.” Mwa chitsanzo, ichi, ngati pali kuya mkati umu, kukuyitana, apo payenera kukhala kuya koti kuyankhire ku kuyitana kumeneko.

Mwinamwake ine ndidzipange ndekha kumveka, monga chonchi. Ndine wokonda kwambiri wa chirengedwe. Ndipo kupita mu thengo, ine ndimayang'ana kulowa kwa dzuwa. Ine ndimamva nyama zikufuula mu nkhalango. Mayi anga ndi theka mmwenye, kotero ndi... Pali chinchake cha izo, mu magazi anga, kuti ine—ine ndimakonda chirengedwe. Ndipo pamene ine ndimva kuyitana kuchokera mu nkhalango, pali chinachake chimayatsa moyo wanga pa moto. Ine sindingakhoze kuchitira mwina.

Kuno, posachedwapa, ine ndinali pamwamba mu Colorado. Ndipo ine ndinali kuyimirira pamwamba pa phiri, ndipo ine ndinali kuyang'ana mayi wamphungu wamkulu pamene iye ankabweretsa ana ake aang'ono kuchokera mu chisa, ndi-pa mapiko ake, ndi kuwakhazika iwo pansi mu msipu wa mauzu. Ndiyeno iye anawulukanso kubwerera pamwamba, pa nsonga pamene pa mwala wawutali kwambiri umene iye akanakhoza kukafikirapo, ndipo iye anakhala pansi. Iye anayamba kuyang'ana. Chabwino, ine ndinali kuyang'ana, kupyolera mu zimagalasi zoyang'anira zanga. Kavalu wanga anali atamangiridwa ku mtengo. Ndipo ine ndinali kuyang'ana. Ndipo ine ndinati, "Ambuye, ine—ine ndikuzikonda izi." Ndipo izo zinkawoneka kwa ine kuti ine ndimakhoza ngakhale kununkhiza...

Ngati inu munayamba mwakhalapo pafupi ndi chisa cha mphungu. Ndipo izo zimamanga icho kuchokera ku mitengo yakuthwa ndi zinthu. Ndipo mphungu zosauka izo zinali kuyenda chabe pa zisonga zimenezo ndi minga, izo sizinali kudziwa kanthu kena kalikonse. Koma tsiku lina mayi mphungu anatambasula mapiko ake, ndipo iwo anaponda pa mapikowo ndipo anapita mmusi.

Tsopano, ine ndinayang'ana pa tiana tating'ono timeneto, ndipo ito tinali kungokhala ndi—ndi chitsitsimutso cha chipentekoste. Ito tinali kumangothamanga chozungulira pa udzu wofewa umenewo, kumangotola apa, ndi kumajomphana pa wina ndi mzake, ndi kumalumpherana pa wina ndi mzake, momasuka basi monga ito tikanakhoza kukhalira.

Ine ndinaganiza, "Chabwino, ndiko kulondola. Tsopano, apo ziri monga munthu mu chisa chakale cha dziko, sadziwa kanthu koma icho chimene Mdierekezi angakhoze kumupatsa iye. Koma tsiku lina Mulungu anamutolapo iye ndi kumukhazika iye pansi mu mthunzi wa msipu wobiriwira. O, momwe iye amasangalalira! Iye ndi womasuka. Palibe kanthu, komupweteka ayi."

Ine ndinaganiza, "Chabwino, nchifukwa chiyani tinthu tating'ono ito sitikuchita mantha? Ndikudabwa ngati ito tikuzindikira kuti kuli ankhandwe pafupi, omwe akanati awatole iwo?" Koma pakapita nthawi iliyonse iwo amakhoza

kuyang'ana mmwamba. Ndipo mayi wamkuluyo anali atakhala pamwamba apo akuwayang'anira iwo.

Ine ndinaganiza, “Chabwino, mayamiko akhale kwa Mulungu! Ndiko kulondola. Iye ananditenga ine kuchokera ku chisa cha mdziko. Ndipo Iye anakwera mmwambammwamba mwa Ulemerero, wakhala Pamwamba apo, akuyang'ana pa cholowa Chake, kuti awone kuti palibe chowopsya chirichonse chikubwera.” Ine ndinaganiza, “Ngati nkhandwe ikanati iwuyambe wopita cha kwa imodzi ya mphungu zazing'ono zija, iye akanati amukwapule iyeyo mpaka kumupha.” Ine ndinaganiza, “Ndiko kulondola. Msiyeni Satana ayambe kutsatira pambuyo pa wokhulupirira, ndipo iye ali naye Yesu Khristu pa manja ake. Ndiko kulondola. Eya. Msiyeni iye atenge. . .” Patapita kanthawi. . .

Iye anali kuyang'ana; mutu wake wawukulu, wachifumu ukuyang'ana pozungulira. Iye anali pa thanthwe lapatali kwambiri limene iye akanakhoza kulipeza, chifukwa iye amakhoza kuwona kulikonse. Maso ake akuthwa a mphungu, akuyang'ana. Ndipo patapita kanthawi, ine ndinamuwona iye akudzutsa mutu wake. Kupyolera mu zoyang'anira zanga za mphamvu khumi, ine ndinamuwona iye akudzutsa mutu wake ndi kuyang'ana mozungulira. Iye anali kukupiza mpweya. Ine ndinaganiza, “Ndi chiyani icho?”

Kutali komwe kumpoto, mpoto unayamba. Bingu linabingula.

Iye anatulutsa mfuu, ndipo pansi kupyola kumeneko iye anapita. Anaponya patsogolo mapiko aakulu amenewo, mpaka ku thengo la mauzu lija. Ndipo imodzi iliyonse ya timphungu tating'ono tija tinathamangira kumeneko mwamsanga kwenikweni; ito tinali titalangizidwa, mwinamwake, asanachoke pa chisapo. Ito tinagwiritsa timapazi tawo tating'ono mu nthenga momwemo. Anaponyera kamwa zawo zazing'ono pansi, mulomo wawung'ono, kuwukowetsa iwo pa nthengazo. Ndipo iye anakwera, ndi gulu ilo la mphungu pa mapiko ake, ndipo anapita molunjika basi, kupyozza mphepo imeneyo, ikuwomba pafupifupi mailosi makumi asanu pa ora pamenepo, kupita mpaka mu mphanga ya thanthwe.

Ine ndinalira ngati khanda. Ine ndinaganiza, “Tsiku lina la ulemerero, pamene chitsitsimutso ichi chiti chidzathe, Iye adzabwera kuchokera ku Ulemerero, kutambasula mapiko Ake aakulu a mphamvu, ndipo mphungu zazing'ono zidzalumitsa milomo yawo mkati mmenemo ndi kuwulukira kutali kupita ku Ulemerero ndi Iye.” Kuya kuyitanira ku Kuya. Ngati kuya kukuyitana, pali Kuya koti kuyankhe.

Mwa kuyankhula kwina, pasanakhale mtengo woti umere pa nthaka, panayenera kuti pakhale nthaka yoti umerepo poyamba. Mulungu sanapange konse mtengo kwa dziko; Iye anapanga

dziko kwa mtengo. Iye anapanga dziko, ndipo analamulira dziko kuti libale mtengo. Ndipo dziko linali kuyitana, chotero mtengo unabwera.

Pasanakhale chipsyepsye pa nsana wa nsomba, panalibe madzi oti iyo izisambiramo. Chifukwa chimene iyo ili ndi chipsyepsye ndi chifukwa panali madzi akuti iyo izisambiramo, kuti izichigwiritsira ntchito icho. Chirichonse chimene ife tiri nacho chiri kwa cholinga ndi kwa chifukwa.

Kuno nthawi yina kale, ine ndinali kuwerenga pamene mnyamata wamng'ono amadya zofutira za pensulo. Iye amadya rabara iliyonse yomwe iye akanakhoza kuipeza. Iye anadya ngakhale pchedulo la pa njinga. Ndipo iwo sanali kudziwa chimene chinali cholakwika ndi mwana wamng'onoyo. Kotero iwo anamutengera iye koti akamupime, kwa dotolo, ku chipatala. Ndipo atatha kumupima iye, iwo anapeza kuti thupi lake laling'onolo linkasowa salfa. Ndipo salfa ali mu rabara, ndipo iye anali kudya rabara kuti apezemo salfa. Tsopano, ndi izi apa. Mvetsani izi. Apo panali. . . Ngati munali chinachake mkati umu choyitanira ku salfa, pamayenera kuti pakhale salfa woti ayankhire ku iko, iye asanayitanire. Mukuona chimene ine ndikutanthauza? Tsopano, pasanakhale apo. . .

“Pamene kuya kuyitanira ku Kuya.” Pasanati pakhale kuya, kukuyitana, payenera kuti pakhale Kuya koti kuyankhire kwa iko. Ndiyeno motsimikiza monga inu anthu, zaka zingapo zapitazo, omwe mwinamwake munali ochimwa. . . Mwina nkukhala kuti munali mu mpingo wina wamawonekedwe, umene sunali kukhulupirira mu ubatizo wa Mzimu Woyera, koma inu munaumva Uthenga. Panali chinachake mkati mmenemo chinkayitanira zochuluka za Mulungu. Inu mwina mukhoza kuti mumakhala mu chikhaliidwe cholungamitsidwa pamaso pa Mulungu, koma inu munkafuna ubatizo wa Mzimu, ndipo inu munkachitira njala yofuna iwo. Tsopano, chifukwa chomwe chakuti kuli Mzimu Woyera, ndi chifukwa chake inu munali kuchitira njala yofuna Iwo. Inu simukanakhala mukuchitira njala yofuna Iwo, kupatula ngati pakanakhala chinachake mkati umu choti chiziyitanira Iwo, kunjira uko. Mukuona chimene ine ndikutanthauza?

Ndipo, ndiye, chifukwa chomwe chakuti inu muli pano usikuuno, inu mukukhulupirira mu machiritso Auzimu. Ndipo ngati akanati asakhale ataphunzitsa nkomwe mu Baibulo, ngati inu gulu la anthu mumakhulupirira mu machiritso Auzimu, payenera kukhala pali kasupe wotseguka kwinakwake kapena inu sibwezi mutakhala nacho chikhumbo cha iwo. Ngati inu muli nacho chikhumbo kuti muchiritsidwe ndi Mulungu, alipo Mulungu woti akuchizeni inu. Ndiko kulondola. Chifukwa, chakuya chimayitanira ku Chakuya.

Ndi momwe izo zinaliri ndi Simioni, iye ankadziwa kuti uko kunali kudza Khristu. Ndipo iye ankadziwa kuti Mulungu anamulonjeza iye kuti iye akanamuwona Iye asanafike iye poti afe. Tsopano zindikirani. Ndiye, munga Simioni anatsogoleredwa...Kodi izo si za chirendo? Pamene Yesu anabwera powonekera kumene, Simioni anatsogoleredwa mwa Mzimu Woyera, kwa Khristu yemwe, mwa Mzimu Woyera womwe unapereka lonjezolo.

Ndipo Mzimu Woyera, Womwe unapereka lonjezo la machiritso Auzimu, wakutsogolerani inu pano usikuuno, ku kasupe yemwe; kumene iye ali wotseguka usikuuno kwa aliyense yemwe afuna, pakali pano, ku Mzimu Woyera womwewo komwe ukutsogolera, ukutsogolera ana aamuna a Mulungu omwe akukhulupirira lonjezo la Mulungu. Inu mukuona chimene ine ndikutanthauza? Mmodzi aliyense wa inu ana aamuna ndi aakazi a Mulungu watsogoleredwa kuno chifukwa inu mukukhulupirira lonjezo la Mulungu. O, pamene ine ndiganiza za izo!

Ndiye ine ndikuganiza, kutali komwe mu ngodya kunali mkazi wachikulire. Iye tikuphunzitsidwa kuti iye anali wakhungu. Dzina lake linali Anna. Iye anali mneneri wamkazi, akuyembekezera kudza kwa Ambuye. Mulungu ali pansu pa chikakamizo kuti amusonyeze iye Khristu. Ndipo Mzimu Woyera unasunthira pa Anna. Ndipo ine ndikukhoza kumuwona mneneri wamkazi wakhungu wachikulireyo mmawa umenewo, akubwera motsatira kudutsa mu nyumbayo, wakhungu, akutsogozedwa ndi Mzimu Woyera, akuyenda motsatira, konseko limodzi ndi anthu amenewo. Kubwera pansu motsatira mzere wa akazi umenewo, ndi kuyima patsogolo pomwe pa kasupe, pakuti iye anatsogozedwa ndi Mzimu Woyera. [Mwinamwake ndi malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

Inde, Iye ali pano usikuuno. Iye wauka kwa akufa. Iye wakupatsani inu lonjezo. Mzimu Woyera wakukokerani inu palimodzi. Ngati inu mukanati musakhale muli pano usikuuno, ngati Mzimu Woyera ukanati usakubweretseni inu pano, inu bwezi muli kunja kwinakwake mu dziko. Koma inu mwakhala pano mu nyumba yotentha ino, mukudzikupiza, chifukwa (bwanji?) inu mukuyembekezera kuti mumuwone Yesu Khristu akubwera powonekera ndi kutsimikizira Mawu Ake. Chiyembekezero!

Ngati inu mukuyembekezera kuti mubwere kuti mudzangopeza chinachake choti muchitsutse, Mdierekezi zedi akusonyezani inu zochuluka kuti muzitsutse. Iye ndithudi atero.

Inu mupeza chimene inu mukuchiyembekezera. Ena a iwo akuti, “Chabwino, palibe, ngati ine ndipeza...ngati ine sindifika mu mzere wa pemphero. Ngati ine nditi ndiwone

chinachake chonga ichi, ndiye ine ndikhulupirira.” Iwe upeza chimene iweyo ukuchiyembekezera.

Ine ndikuyembekezera, usikuuno, kuti ndiwuone Mzimu Woyera utabwera ndi kudziwonetsera Iwowokha mu mphamvu, kutsanulira Ulemerero Wake, mu nyumba iyi kuno; ambiri alandire ubatizo wa Mzimu Woyera; ochimwa azilira pa njira yawo akupita ku Kalvare; odwala kukhala akuchiritsidwa; mitundu yonse ya zizindikiro ndi zodabwitsa. Chifukwa, Yesu Khristu wazilonjeza izo, ndipo ine ndikukhulupirira lonjezo Lake.

Tiyeni tipemphere ife.

Atate Akumwamba, monga Mawu Anu ali Choonadi, tsimikizirani Mawu Anu ndi zizindikiro ndi zodabwitsa za Yesu wowukitsidwa. Ife tikudziwa kuti pamene Iye anali pa dziko lapansi, Iye sankadzinenera kuti anali munthu wamkulu, Iye ankangodzinenera kuti Inu munkamusonyeza Iye masomphenya, choti achite. Iye ankadziwa malingaliro a anthu, zikhalidwe zawo. Iye anadziwa pamene mkazi, anali ndi vuto lotaya magazi, anali atakhudza chovala Chake. Iye anali atayima panja pamenepo, ndipo iye anawona kuti iye sakanakhoza kukhala atabisika, pakuti Yesu anali akuyang’ana kumene pa iye. Iye anadziwa. Iye anati, “Chikhulupiriro chako chakupulumutsa iwe.”

Ndipo, Atate, ife tikudziwa kuti Iye ali pano usikuuno, chifukwa Iye analonjeza kuti atero. Ndipo chidaliro chathu chazikika mwa Iye, mu Mawu Ake. Ife tikutsimikiza. Ife tamuwona Iye mu makwaniritsidwe a chiwukitsiro Chake chachikulu, pano pa dziko lapansi, akugwira ntchito pakati pa anthu Ake, mu mpingo Wake. Ndipo, Ambuye, tiloleni ife tikhale, lero, opereka-Kuwala ku m’badwo uno. Kutu, pamene seweru lalikulu liti lidzayikidwe pamapeto a msewu, ndipo aliyense wa ife kubwera mpaka pamaso pa Inu, ndipo chowonetserapo chachikulu chitasololedwa, ndi miyoyo yathu ya m’badwo uno itabweretsedwa pamaso pathu, Mulungu, ndiroleni ine ndidzambe liwu langa likutsutsa kusalungama, ndi kuyitanira kwa anthu kuti akhulupirire pa Yesu, Mwana Wanu.

Dalitsani anthu pano usikuuno. Iwo akhala mu kutentha kwakukulu. Ndipo ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu muwapatse iwo mdalitso wapadera. Mulole mphamvu zotonthoza za Mzimu Woyera zichotse malingaliro onse a izi.

Ndipo, Ambuye, muyeretseni wantchito Wanu pakali pano, chifukwa cha utumiki umene uli kudza. Ndayima pano, ndikuzindikira kuti maso atembenezidwira mmbali ino. Ndipo ine ndikupemphera, Atate, mwa kudzichepetsa, kuti Inu mulola Mphamvu Yanu yayikulu, yaulemerero idziwike kwa aliyense. Ndipo ngati wantchito Wanu wosayenera wapeza chisomo pamaso Panu, kwa usikuuno, Inu mutamutenga munthu

wosayenera uyu, chotsanipo umunthuwo, ndipo bwerani mkatimo, Ambuye Yesu, ndi kuyankhula kwa anthu Anu.

Ndipo pamene moyo uli utatha wonse, pano pa dziko lapansi; pemphero lotsiriza kukhala litapempheredwa, nkondo zonse kukhala zitachitika, utsi utawuma, utapita, zida zitawunjikidwa, Mabaibulo atasekedwa, ndipo ife titabwera ku nyumba Yanu; mmawa wawukulu uwo kutulukira, Mwamuyaya, wowala ndi wabwino. “Ndipo pamene osankhidwawo ati adzasonkhanire ku Nyumba kwawo kuseri kwa milengalenga,” wandakatulo anatero. Ambuye, pamene ife tidzawona gome lalikulilo litayikidwa kunja uko, ku mgonero umenewo, mailosi zikwi utali wake; kuyang’anizana pa gomelo kwa wina ndi mzake, ankhondo akale a zipsyera, misozi ya chimwemwe ikutsikira pansi pa masaya athu. Mfumu kutulukira uko, kukongola Kwake, chiyero, kuyendera pansi motsatira gomelo, ndi kutenga manja Ake Omwe ndi kumaipukuta misonzi kuichotsa pa maso awo, akuti, “Musati muziliranso. Zonse zatha. Lowani mu zisangalalo za Ambuye.” Zovutikira za ulendo sizidzawoneka ngati kanthu pamene, Atate, pamene ife tidzafika pa mapeto a ulendo.

Ndipo tithandizeni ife usikuuno, Ambuye, kuti tiyiwale zinthu izo zomwe ziri zakale, tiroleni ife tilimbikire kupita ku malo a kuyitana kwa pamwamba tsopano. Ndipo mulole Mzimu Wanu ubwere ndi kuwonetsera Mwana Wanu wamwamuna, Yesu Khristu, kwa anthu awa. Monga, ine ndayesera, monga wa chivundi, kuti ndiwauze iwo za Inu kuti ndinu yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse. Pakuti, ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu, mwana Wanu wokonedwa. Amenii.

Ambuye akudalitseni inu. Ndipo usikuuno, usanayambe utumiki wa machiritso...Mundikhululukire ine chifukwa chokhala khanda, koma pali chinachake chimene chimafika mu mtima wanga pamene ine ndiyankhula za Iye.

Ine ndikukumbukira pamene ine ndinayitanidwa koyamba, ndi atumiki anga, pamene iwo anawona...Chiyambireni ndiri mwana wamng’ono, masomphenya amakhoza kubwera. Iwo ankati, “Billy, usati iwe uzipita konse ku zimenezo.” Ankati, “Ameneyo ndi Mdierekezi.” Pokhala ndikuphunzitsidwa izo ndi azibusa, ine mwatheka ndinkakhulupirira kuti masomphenyawo akanakhoza kukhala olakwika.

Ndiye pamene Iye anabwera kwa ine usiku umenewo ndi kundiuza ine Yemwe Iye anali! O, mai! Ndipo ine ndikudziwa kuti Iye ali pano pakali pano. Ndipo ine ndimakudziwa Kukhalapo Kwake. Ndipo ine ndikudziwa kuti ine ndimamukonda Iye. Ine ndinkaganiza, “Ine ndikanakhoza bwanji kukhala Mdierekezi, ndi kumamukonda Ambuye Yesu momwe ine ndikuchitiramu? Motani? Mtima wanga ungakhoze bwanji kumawukhira kwa Iye...Ndipo Iye akuudziwa mtima

wanga.” Ndipo Iye anabwera ndipo anandiuza ine zosiyana. Ine ndikumukhulupirira Iye, chifukwa Izo zikugwirizana ndi Mawu a Mulungu. Ndipo mawu awo sagwirizana ndi Mawu a Mulungu, pakuti ife tikukhala mu tsiku lino.

Ndipo tsopano, abwenzi Achikristu, ine ndikufuna kuti ndinene kwa inu nonse; chifukwa, pamene Iwo undigunda ine, nthawizina inu mukhoza kudabwa chimene chinachitika. Ine—ine sindingakhoze kufotokoza izo. Ndi zopitirira ine kuzifotokoza. Koma ine ndimafooka kwambiri kuti ine sindingakhoze kuyima nkomwe, pambuyo pa mwina munthu mmodzi kapena awiri amene ine ndimakomana nawo. Inu mwina simungakhoze kumvetsa zimenezo, koma, ingowerengani Lemba, Ilo limafotokoza izo. Ine ndikumukhulupirira, mneneri Daniele anali atawona masomphenya; iye anati iye anavutika ndi mutu wake kwa masiku ochuluka. Ndi kulondola uko?

Ndipo Yesu, nthawi yina, pamene mkazi, wokhala ndi chikhulupiriro chokwanira kuti amukokere Iye chozungulira ndi kumuwona yemwe iye anali, Iye anati, “Ine ndazindikira kuti ukoma, mphamvu, zachokwa mwa Ine.” Ndipo anthu uko komwe, pamene . . .

Si ine ayi, Akristu. Ayi. Ine ndiri . . . Ine ndine munthu chabe, mkulu wa ochimwa. Koma, mmodzi wobadwa mu nyengo yake, kwa inu anthu a Uthenga Wonse. Ndiko kulondola. Mwa chisomo, mwa chisomo cha Mulungu, Iye wandirola ine kumakutchani inu abale anga ndi alongo. Ndipo ine—ine ndimakukondani inu.

Ndipo ine—ine sindiri pano usikuuno kuti ndiwonedwe kapena kumvedwa. Ine sindiri pano chifukwa cha ndalama. Izo, ine . . . Inu mukudziwa zimenezo. Kotero ine ndiri pano kwa chinthu chimodzi, chifukwa ine ndimamukonda Yesu ndipo ine ndimakukondani inu. Ndipo ine ndikumukhulupirira kuti pa kubwera, mwa kuyitanidwa uku, mwinamwake ine ndingakhoze kudzipereka ndekha kwa Iye ndipo Iye angachite chinachake kupyolera mwa ine, chimene chingakupangeni inu mukonda Iye mochulukira, ndi kumukhulupirira Iye ndi kuchizidwa. Ndicho (mai) chodalira chokha chimene ine ndinali nacho, chakukhala pano.

Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu azibusa kachiwiri, ndi amuna amalonda. Ndipo ine ndikunena kwa inu tsopano, ine ndisanafike pfooka kwambiri; nthawizina ine ndimalephera kuchoka pa nsanja. Mnyamata wanga ndi manenjala, ndi iwo, amayang’anira zimenezo. Ndipo ine ndikufuna kuti nditi tsalani bwino kwa inu. Ndipo Mulungu akudalitseni inu. Ndipo ngati ine sindidzawonana nanu konse inu kenanso mbali ino ya mtsinje wawukulu uwu, ine ndidzakuwonani inu mmawa, kumene . . . Ndipo ine ndidzakhala

nawo umboni umene ine ndiri nawo tsopano: ine ndimamukonda Ambuye Yesu.

Ndipo, masomphenya, Mulungu wandipatsa ine masomphenya. Izo ndi zooni; Baibulo liri patsogolo panga, ndi Mulungu Yemwe ali mboni yanga, ndipo akudziwa. Ndipo ine ndingakhoze kokha kufotokoza ndi kunena monga Iye angati andirolele ine, mwa chisomo Chake, kuti ndichite. Kotero, mundipempherere ine.

Ndipo chinthu chimodzi chinanso chimene ine ndikufuna kuti ndifunse. Ine ndikupita ku Afrika, India, Palestina, Germany. Ndipo, kumbukirani, mu mayiko amenewo, monga izo zinali kale; musaganize kuti asing'anga ndi anthu onse awo ogwidwa ndi ziwanda angakutsutse iwe mpaka kukugwetsa, ndipo iwe uyenera kumadziwa chimene iwe ukuchikamba. Ndiko kulondola. Ndipo pamene mphepo zikuwomba, motantha ndi mwamphamvu, ndi kuzunza kukuchitika, ndipo ine ndizikakumbukira, mu Washington, D.C., kuti winake akundipempherera ine. Kodi inu mungandilonjeze ine izo? Ngati inu muti mutero, kwezani... [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi.] Zikomo inu. Mulungu akudalitseni inu. Zikomo inu kwambiri.

Tsopano, ine ndikuganiza, usiku watha iwo anapereka makadi a pemphero zana, usiku watha. Ndipo ine ndikukhulupirira nambala imeneyo inali... kapena chilembo chimenecho chinali Y. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti ine ndinayitana oyamba khumi ndi asanu a iwo, usiku watha. Ine ndikuganiza uko nkulondola. Sichoncho izo, abale? [M'bale akuti, "Ndiko kulondola."—Mkonzi.] Khumi ndi asanu oyamba a makadi awo omwe anaperekedwa.

Tsopano ife tiyitana ena ochulukirapo a iwo. Ndipo mwinamwake, usikuuno, ngati chikhulupiriro chiti chibwere mokwera, mwinamwake ife tikhoza kutenga magulu awiri kapena atatu a iwo. Ndipo ngati ayi, ine ndikupempha munthu aliyense pano... Ndi anthu angati mkati muno omwe alibe khadi la pemphero ndipo akanafuna kuti achiritsidwe ndi Mulungu usikuuno? Ingokwezani dzanja lanu; amene alibe khadi la pemphero. Chabwino, ndi basi... Iwe sungakhoze kudziwa basi. Angokhala molimba, kulikonse.

Ine ndikuti ndikufunsi inu chinachake. Iyi ikhoza kukhala mwinamwake nthawi yanga yoyamba yomwe ndakumanapo nanu inu. Ndi zoyipa kwambiri kuti ife sitingakhoze kukhala motalikitisa pang'onopo mu msonkhano ndi kuti inu mudziwe momwe mungavomerezere machiritso Auzimu. Auzimu...

Ndipo nthawi zambiri, pamene anthu achizidwa... Chophuka ndi—ndi chiwanda. Matenda aliwonse ndi a Mdierekezi. Mulungu sangakhoze, sangati ayike matenda pa

ana Ake. Mdierekezi amachita zimenezo. Mwaona? “Ndipo ngati Satana atulutsa Satana . . .”

Inu mukuti, “Bwanji, Mdierekezi amachiza, nayenso.”

Chabwino, Yesu anati iye sangakhoze. Iye anati, “Ngati Satana atulutsa Satana, ufumu wake wagawanika.” Koteri, iye sangakhoze. Mulungu yekha angakhoze kuchiza.

Mankhwala ndi adotolo samadzinenera kuti angachize. A Mayo Apachibale ndi amodzi a olamulira athu opambana. Iwo anati, “Ife sitimadzinenera kuti tingachize.” Anati, “Ife timangonena kuti timathandizira chibadwa.”

Pali mchiritsi mmodzi yekha, ndiye Mulungu. Iwo akhoza kusoka pa malo, mu dzanja lanu, koma iwo sangakhoze kupachiza ipo. Iwo akhoza kungopasoka apo. Wa zamano akhoza kuzula dzino, koma ndi ndani yemwe ati achize pa malowo? Dokotala akhoza kuchotsa kathumbo, koma ndi ndani yemwe ati achize malo omwe iye anadulapo? Mulungu amachiza. Mankhwala samamanga minofu. Mankhwala ali othandizira kokha. Mulungu ndiye mchiritsi. Dokotala akhoza kuwukonza mkono wanu, koma, pamene iye abwera ndi kudzawukonza mkono wanu, ndipo inu nkusatuluka . . . Ndipo inu nkusakhala bwino. Dokotala wachita gawo lake, zomwe iye anaphunzitsidwa kuti azichita, ndi chidziwitso chochitira. Iye amakonza mkono wanu, koma iye amazisiyira izo kwa Mulungu kuti achize. Ndiko kulondola. Kuchiza konse ndi kwa Mulungu. Koteri, tsopano, inu mungomukhulupirira Iye.

Ndipo nthawizina pamene zithupsya zimenezo, moyo ukachoka mwa izo, monga chiwanda, chabwino, ndiye zithupsya zimenezo zimafa.

Ngati moyo ukanachoka mwa inu, ndithudi, inu mukanafa. Moyo wanu ukanachoka mwa inu, koma thupi likanali pomwepo. Ilo limafota. Ngati pali oyikitsa maliro pano, akudziwa kuti thupi laumunthu . . . Thupi lililonse- . . . Mnofu uliwonse umafota pamene moyo uchokamo. Ipenyeni nyama yaing’ono pamene—pamene iyo iphedwa pa msewu. Iyo imalemera . . . Kapena, ena a inu asaki pano, ngati inu mupha nyama, yang’ombe, kapena yogulitsa; ndipo inu mukayiika iyo pa muyezo ndi kuyiyeza iyo tsopano, mungoyipha iyo ndi kuyiyeza iyo. Ndiye, mmawa, muyiyezenso iyo kachiwiri ndipo muwone ndi mapaundi angati kupepukira iyo ili. Ndiye muyilole iyo igone pamenepo kwa masiku awiri kapena atatu, ndiyeno muwone kuti ndi mapaundi angati iyo ili yolemerera.

Chabwino, tsopano, chithupsya, pamene icho chifa, chiwanda chimatulukamo mu chithupsyacho, monga chammimba, khansara, ng’ala, zina zotero. Pamene chiwanda chituluka mwa izo; womwe uli moyo.

Munthu aliyense pano anabwera kuchokera ku nyongolosi imodzi yaing’ono, ndipo—ndipo inu mumayamba kukula

makhungu. Ndipo makhungu amenewo anabwera mkati monga mwa chibadwa cha moyo umene unali mwa iwo, umene unapanga munthu. Ndipo makhungu ochokera kwa garu amapanga garu; ndipo a mbalame mbalame. Chirichonse monga mwa chirengedwe chake, mtundu uliwonse.

Koma tsopano, chiwanda, chimene chiri chithupsya, kapena icho sichisowa kubwera mu chithupsya, ndicho... chimayamba kupanga makhungu. Titi, mwachitsanzo, khansara. Iyo imayamba kupanga makhungu, ndipo imayamba kukulira, kulira. Chabwino, tsopano, iyo ili nawo moyo, ndipo ili yamoyo.

Mofanana basi monga inu munali amoyo ndi kumakula mu chiberekero cha amayi anu. Chinthu chomwecho, inu mukukula.

Koma, tsopano, moyo umenewo sindiwo moyo wanu, ndi moyo wosiyana. Inu muli nawo moyo, woti mukhale moyo; ndipo uwo ndi moyo wa imfa, kapena mzimu wa imfa, kani. Mundikhululukire ine. Ndipo ndi imfa. Chabwino, tsopano, iwo suli wa mwa inu. Iwo sunali mmenemo poyamba, koma iwo uli mmenemo tsopano. Chabwino, ndiye, ndani anawuyika iwo mkati mmenemo? Iwo uyenera kubwera basi kuchokera ku chinthu chimodzi, ndiye Mdierekezi. Ndipo iyo ndi nyongolosi. Khansara, chotupa, chirichonse cha zinthu zimenezo, zinabwera kuchokera ku nyongolosi. Ndipo inu munabwera kuchokera ku nyongolosi, inunso, mwaona.

Kotero pamene izo zinafa, mwa chitsanzo, monga ng'ala. Munthu yemwe ali ndi ng'ala, pamene mzimuwo uchoka, anthu amati, "O, ine ndikukhoza kupenya! Ine ndikukhoza kupenya!" Ndipo tsiku lotsatira, iwo amakhoza kuwona bwino kwambiri. Koma ndiye pafupi, pakatha pafupi maora makumi asanu ndi awiri mphambu awiri, chivundi chimalowamo.

Monga chiwukitsiro cha Yesu, tsopano, makhungu sanavunde. Iye anawuka asanafike masiku atatu ndi usiku, ndithudi. Inu mukuona, Iye anafa Lachisanu madzulo, ndipo anawuka Lamlungu mmawa. Chifukwa, Davide anati, "Ine sindidzasiya moyo Wake mu hade, ngakhale kulola Mmodzi woyera Wanga kuti awone chivundi."

Makhungu amenewo amayamba kusweka mu maora makumi asanu ndi awiri mphambu awiri. Ndipo pafupi... Ndiyeno pamene wodwala... Pamene icho chiyamba kufufuma, chithupsya chimenecho, kuyamba kukulira, iwo... Ndithudi mtima wanu uyenera kutsuka mtsempha wa magazi.

Dona anabwera kwa ine usiku watha, woyera kwambiri, mkazi wowoneka-mwaumulungu, ali ndi khansara wamkulu yemwe... Iye anati iye anabwera mu mzere, ndipo anati iye anali yense ataphimbidwa, tsitsi lake. Ndipo anati ine ndinayima ndi kuyang'ana pa iye, ndi kumuwuza iye, pansu pa Mzimu, iye anali ndi khansara mu mutu wake. Ndipo ine ndinati iyo ichokamo. Ndipo iyo inachoka. Ndipo iye ali nayo iyo pano, ine

ndikuganiza, usikuuno, kuno mu botolo la kachaso, pomwe pano tsopano. Ife takhala tiri nawo zikwi za izo.

Kodi mkaziyo ali mu nyumba ino? Kodi iye angayimirire, ngati mkaziyo ali paliponse mu nyumba ino, ali ndi khansara mu kachaso uja. Ngati iye ali paliponse mu nyumba muno, ngati iye waimirira, gwedezani dzanja lanu kapena chinachake, kuti wina akhoze kukuwonani inu. Eya. Ndi uyo dona wayima apoyo, yemwe ali ndi khansara.

Ndipo ine ndawawonapo iwo, atayima pa nsanja, nkungosanduka yoyera ndi kugwera pa nsanja apo pomwe. Mwaona? Tsopano, ndicho chozizwitsa.

Kawirikawiri, pamene chithupsya chafa, moyo umatuluka mwa icho. Koma, chithupsyacho, ngati icho sichingakhoze kugwa, icho chiri mkati. Ndipo ngati icho chitero, ndithudi, icho chikhala chiri pamenepo kwa masiku angapo ndi kuyamba kutupa. Monga mnofu wina uliwonse, makhungu amayamba kusweka. Ndiye iwe umayamba kudwala kwambiri ndi malungo. Ndithudi, ndi kudwala, ngati. Mtima umapompa magazi ndi kulitsuka thupi. Pamakhala nchini yayikulu ya mnofu uli womasuka mu thupi lanulo. Wodwalayo amayamba kudwalika kwambiri.

Ndiye inu mukati, “O, ine—ine ndinamverera bwino kwambiri pamene ndinali pa nsanja, ndipo kwa tsiku kapena awiri. Koma ine ndikuganiza ine ndataya machiritso anga.”

Bwanji, m'bale, mlongo, ndicho chizindikiro chopambana mu dziko kuti iwe walandira machiritso ako. Mwaona? Ndiyeno inu mukayamba kusakhulupirira, ndipo, basi motsimikiza momwe chikhulupiriro chanu chinachotsera moyowo, kusakhulupirira kwanu kuwabweretsanso iwo kachiwiri. Mwaona? Iko kuteru. Iko kuwawukitsa iwo. Kumbukirani, Yesu anati, “Pamene mzimu wosayera utuluka mwa munthu, iwo umakayenda mu malo owuma, ndiye iwo umabwerera ndi mizimu yina isanu ndi iwiri.” Ndi kulondola uko?

Ndipo chotero muloleni mwamuna wabwino wa nyumba, chikhulupiriro, akhale pamenepo, ziribe kanthu momwe inu mukumverera. Si chomwe inu mukumverera; ndi chomwe inu mukukhulupirira. Yesu sananenepo kuti, “Kodi inu munazimverera izo?” Iye ankati, “Kodi inu mwakhulupirira izo.” Ndi zimenezotu. Mulungu akudalitseni inu. Chabwino.

Tsopano, tiyeni tiwone, ine ndikukhulupirira kuti aja anali makadi apemphero zana limodzi amene iwo anapereka usiku watha, mu Y. Ife sitinafike kwa onse a iwo. Tiyeni titenga khumi ndi asanu otsiriza a iwo usikuuno, kuti tiyesere. Ndani ali ndi khadi la pemphero eyite-... Limenelo lingakhale, ayi, eyite-faifi. Ndani ali ndi khadi la pemphero 85? Kodi inu mungakweze dzanja lanu, ngati winawake pano, penapake kumbuyo, khadi la pemphero eyite-faifi.

Chabwino, eyite-sikisi, ndani ali ndi khadi la pemphero eyite-sikisi? Chabwino. Eyite-seveni, eyite-seveni, kodi ine ndikumuwona winawake ali ndi khadi la pemphero eyite-seveni chonde? Ngati inu . . . Kodi inu mungayime, eyite- . . . Chabwino, eyite-seveni ndi omwe . . .

Onani, winawake mwina sangakhoze kuyima; mwinamwake iwo ali pa machira; mwinamwake iwo ndi ogontha; ndipo—ndipo iwo amati, “Chabwino, palibe aliyense anandithandiza ine.” Ndipo ine—ine ndimalandira kubweza kwa moto kwa izo, mu ofesi yanga. Iwo amati, “Chabwino, ine ndinali kumene kuja. Ndipo—ndipo inu munangoti kuchokera pakuti-ndi-pakuti mpaka pakuti-ndi-pakuti, ndipo palibe yemwe anandithandiza ine.” Ndipo mwinamwake iwo anali ogontha.

Tsopano penyani. Ife tiri ndi eyite-faifi, eyite-sikisi, eyite-seveni. Yang’anani pa khadi la woyandikana nanu ndi kuona. Iye mwina akhoza kukhala wogontha ndipo sangakhoze kumva. Eyite-seveni. Zikomo inu, mlongo. Eyite-eyiti, ndi ndani ali ndi eyite-eyiti? Khadi la pemphero eyite-eyiti, kodi ali mnyumba muno? Eyite-eyiti? Chabwino. Eyite-naini, ndi . . . ali ndi khadi la pemphero eyite-naini? Kodi inu mungayimirire? Eyite-naini, kodi dzanja lakwezedwa la eyite-naini? Chabwino, eyite-naini. Chabwino, nainte, nainte?

Kungo khulupirira, mwabwino chotero tsopano.

Tsopano, ndi aliyense muno, ngati inu muti mungochita tsopano chimene Iye anena kuti muchite. Tsopano, ziribe kanthu chimene Iye ati chiyani, inu muchichite icho. Ingochitani izo. Basi—inu mungopita kukachita chimene Iye ati muchite.

Tsopano, ndine m’bale wanu, ndi munthu chabe. Tsopano ngati Iye ati abwere ndi—ndi kudzatenga chimango chosauka ichi, ndi kuchidalitsa icho mokwanira, kuti lilole Mzimu Wake Woyera ugwire ntchito kupyolera mu ilo, ndiye inu mumuwona Yesu Khristu akuyenda mwa omvetsera.

Ndipo, tsopano, ziribe kanthu mochuluka bwanji momwe Iye ati adzitsimikizire Iyeyekha pano, ngati inu simuli kukhulupirira Iye, Iye sangakhoze kukuchitirani kanthu inu. Ndi kulondola kumeneko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Ziribe kanthu ngakhale Iye akanati ayime pomwe pano pa mbali yanga, mowoneka, mwakuti inu nkukhoza kumuwona Iye, chabwino, ngati inu mutapanda kundikhulupirira ine, ine sindikanakhoza kukuchitirani inu kalikonse. Koma anga—mawu anga angokhala basi chimene Iye wanena kuchokera mu Lemba, ndipo ine ndipemphera ndi mtima wanga wonse kuti Mulungu akuthandizeni inu. Chifukwa, mukhala muli mwinamwake amayi ndi abambo, ndi ena otero, muno, omwe ali odwala ndi osautsika, ndi osowa. Ndipo ine ndimupempha Mulungu kuti akuthandizeni inu, mwakukhoza kwa kudziwa kwanga.

Chabwino, folani apa cha kumanjaku.

Tsopano tiyeni tonse tiweramitse mitu yathu mphindi chabe.

Atate achifundo, ife tikupemphera mu dzina la Mwana Wanu Yesu, mulole Mzimu Woyera ubwere tsopano ndi kudzakwaniritsa ntchito za Yesu Khristu. Adalitseni anthu awa, paliponse, ndipo apangeni iwo kuti akhale athunthu, achizeni iwo, apangeni iwo kukhala bwino, okondwa.

Ndipo tsopano, polinga kuti tichite izi, Atate, Inu mukudziwa kufooka ndi...Wanu...kwa wantchito Wanu. Ndipo ine—ine sindikudziwa choti ndinene kapena choti ndichite. Ndipo tsopano ine ndachita izi zonse mwa kulamulira Kwano, ndipo ine ndikukulupirira kuti Inu mukhala pano, usikuuno, kuti mudalitse ndi kuwathandiza anthu awa. Ndipo, Atate, ngati Inu mungowulola Mzimu Woyera kubwera kwa wantchito Wanu ndi kuwulula zinthu izi kwa ife, zomwe ife tiyenera kuchita, ndi momwe ife tiyenera kuchitira izo, ndiye ife tonse tidzakhala okondwa ndi osangalala. Ndipo omvetsera awa akhulupirira pa Inu, ndi mtima umodzi ndi chigwirizano. Ndipo, Atate, ine ndikukupemphani Inu izi, monga wantchito Wanu, musati mulole munthu mmodzi wofooka achoke mnyumba ino usikuuno. Mulole iwo, mmodzi aliyense, apite wabwino ndi wathanzi, ndipo akusangalala. Chitani izo. Kodi Inu mutero, Atate? Ine ndikupemphera ndi chisomo mu mtima wanga, ndi chikhulupiriro, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

Tsopano, nthawi zambiri...Eya, kodi alipo winawake pa nyali izo, winawake pa nyali, yemwe angakhoze kuzisuntha izo?

Tsopano, nthawizina, Mzimu Woyera uwu, Iwo umabwera...Ndipo ambiri a inu mwachiwonapo chithunzi. Ngati ine nditi ndidzabwerenso konse, ine ndidzakubweretserani zina za izo, monga M'bale Moore anali kunena usikuuno. Ichu chajambulidwa nthawi zambiri. Ndipo mu mabuku...Ine ndikuganiza inu nonse muli nawo iwo. Ife...ine ndinali nawo mabokosi awiri okha, kotero ine ndikuyembekeza inu musangalala nawo iwo mwabwino kwenikweni. Ndipo tsopano iwo...Inu muyang'ane mmenemo ndipo inu muwona chithunzi china cha Iwo, pamene Iwo unali kukhazikika pansu. Ndipo wojambula wa nyuzipepa anachijambula icho, ku Camden, Arkansas, koma icho sichinali chovomerezeka monga cha American Association ichi. Ndipo iwo—iwo anali nacho icho, ndipo panali apo pamene icho chinadzakhala chovomerezeka. Kotero ife...Ndipo zikwi zambiri za anthu...

Ine ndinali kuyima pa mtsinje, kuno nthawi yina kale, ndikubatiza mazana asanu chitachitika chitsitsimutso, ndipo Iwo unabwera pansu pomwe kumene ine ndinali kuyimirira. Ndipo anthu anakomoka, ndipo basi iwo unali pamene.

Ndipo Iwo unali basi ngati kubangula kwa phokoso ndi Moto wopokosera.

Ine ndikupemphera kuti Mulungu abwere mowoneka pamaso pa omvetsera usikuuno, mwa njira imeneyo, kuno ku likulu, kamodzi kenanso, ngati ine ndingapeze kukondedwa ndi Mulungu.

Tsopano, inu mukuzindikira, Iwo ukhoza kubwera kwa maso ena, ndi kusatero kwa ena. Ife sitifuna kuganiza choncho, koma Iwo umatero.

Yohane anali mmodzi yemwe anachitira umboni, wa kuona Mzimu wa Mulungu uli pa Yesu. Ndi kulondola uko? Sanati konse, “Omvetsera.”

Ndipo—amuna anzeru anatsatira nyenyezi. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Ndipo Iyo inadutsa pamwamba pa zoyang’anira mmwamba zonse mu dzikolo, njira yonse kuchokera kummawa, masabata ndi miyezi, akubwera. Ndipo iwo ankatchera nthawi ndi nyenyezi. Iwo ankayang’anira, utali wa usiku wonse, ndipo ankasunga nthawi, ndipo palibe mmodzi anayiwona iyo. Koma amuna anzeru anayiwona, pakuti iwo anali kuyembekezera izo.

Inu mukhoza kumamuyang’anira Khristu usikuuno, ndipo inu mumuwona Iye. Ambuye Yesu akudalitseni inu! Chabwino.

Billy Paul, M’bale Moore, ena a inu, ali...yense yemwe wakonzeka. Chabwino. Kodi iwo afoletsa kale mzere wonse, Billy, khumi ndi asanu onse? Onse khumi ndi asanu afoletsedwa.

Tsopano, kwa ena a inu, yesani iwo amene alibe khadi la pemphero ndipo inu mukudziwa kuti simukhala mu mzere. Ine ndikufuna inu kuti muyang’ane mbali ino ndi kumangokhulupirira. Ndipo inu mukhulupirire mwa mtundu womwewo wa chikhulupiro cha mkazi uja yemwe anakhudza chovala Chake.

Ndipo Iye anatembenuka ndipo anati, “Chikhulupiro chako chakupulumutsa iwe.” Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye ali chimodzimodzi usikuuno? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi inu mukukhulupirira...

Mu gulu lonse lofuula ilo, mwamuna wamng’ono wosauka uja atakhala pansu pa makoma a Yeriko, mwinamwake kawiri utali wa nyumba ino, akukuwa ndi kufuula, “Ndichitireni ine chifundo!” Yesu mwinamwake sanamve konse kuyitana kwake.

Koma Iye anamverera chikhulupiro chake. Icho chinasuntha. Mu gulu lonse ilo la otsutsa! Ndipo Iye anatembenuka, ndipo anati, “Chikhulupiro chako chakupulumutsa iwe.”

Iye anatembenukira kwa omvetsera, ndipo ananena mosiyana. “Nchifukwa chiyani inu mukulingalira mu mtima mwanu?” Ananena kwa mkazi wa pa chitsime,

“Pita ukamutenge mwamuna wako.” Ndipo Iye anati, “Ine sindingakhoze kuchita kanthu kupatula Atate akandisonyeza Ine.” [Msonkhano wa usikuuno watha—Mkonzi.]

[Msonkhano wa usiku wina uli mu kuchitika motsatiramu—Mkonzi.]

Ine ndikukupemphani inu chinachake. Ngati chimene ine ndanena chiri choonadi, ngati icho chiri choonadi, ndiye Mulungu ali wokakamizika ku Mawu Ake. Osati kwa ine, koma ku Mawu Ake. Ndi kulondola uko? Iye ali wokakamizikira ku Mawu Ake. Ndipo, ndiye, Iye azifikitsa izo pochitika chimodzimidzi basi momwe Iye ananenera kuti Iye akanadzachita izo. Ndipo ngati Iye ati achite izo, kodi nonse a inu muli muno ndiye, ngati simunalandire Yesu Khristu, kodi inu mudzakhala ololera kuti muchite izo?

Ndi inu omwe muli pano, omwe mungakhoze kuwona chifundo Chake kwa ena, eya, Iye achita chifundo kwa inu ngati inu mungokhala nacho chikhulupiriro ndi kukhulupirira. Ingo pempherani ndi kuti, “Ambuye, ine—ine ndine wokhulupirira, ndipo ine ndikufuna Inu kuti mundichize ine usikuuno.” Ndipo Mulungu azichita izo.

Ife tangochoka kumene ku Afrika, posachedwapa, kumene ine nditi ndibwerereko mu masabata angapo otsatira. Afrika, India, Palestina, Germany ndi ku utumiki. Ndi ku Durban South Afrika, atatha pafupi anthu atatu kapena anai kudutsa kupyola mzere wa pemphero, ndipo iwo atawona mphamvu ya Mzimu Woyera ikuyenda mwa anthu, ndi kuwona chimene Mulungu anali kuchita, zikwi makumi atatu analandira Yesu ngati Mpulumutsi wawo mu kuyitanira paguwa kumodzi. Zikwi makumi atatu pa nthawi imodzi.

Kotero, ine ndikukhulupirira, ngati ife titi titenge Mawu a Mulungu ngati muyezo, ndi kupita mu dziko lonse ndi kukalalikira Uthenga! “Uthenga sunadze mu Mawu okha, koma kupyolera mu mphamvu ndi chiwonetsero cha Mzimu Woyera.” Kotero, u—Uthenga, ndiwo kuwonetsera kwa mphamvu ya Mzimu Woyera.

Ine ndapita mu mayiko. Iwo amati, “Tsopano, ife sitikufuna misionare. Ife tikudziwa zambiri za izo kuposa momwe inu mukuchitira. Koma, chinthu chimene ife tikuchifuna kuti tichiwone, ndi winawake yemwe ali nacho chikhulupiriro chokwanira kuti apangitse Mawu a Mulungu kuwonetseredwa.”

Ndicho chimene iwo akufuna kuti achiwone. Ndipo ndi momwe iwo amatembenukira. Ndi momwe iwo amamupezera Khristu, ndi chifukwa iwo—iwo amakhulupirira mwa njira imeneyo. Ndipo ine ndikudalira kwa Mulungu, ndi mtima wanga wonse, kuti akhalapo ambiri, ambiri pano usikuuno omwe ati amupeze Khristu chimodzimidzi kwa mtima wawo. Mulole

Ambuye Yesu, waku Nazareti, adalitse wina aliyense wa inu, ndilo pemphero langa.

Tsopano, mwakonzeka?

Palibe munthu amafunafuna Mulungu pa nthawi iliyonse. Mulungu amafunafuna munthu. Palibe pamene munthu anayamba wafunafuna Mulungu, mu dziko lonse. Mulungu akufuna munthu. Pamene munthu anagwa poyamba, mu munda wa Edeni, izo zinasonyeza kachitidwe ka munthu. Munthu anabisala; Mulungu anali akumufunafuna munthu, Yesu anati, “Palibe munthu angakhoze kudza kwa Ine kupatula ngati Atate Anga amukoka iye.” Iye ayenera kukokedwa ndi Atate, choyamba.

Ndipo, ndiye, ine ndikanakonda kuti ndifotokoze chinachake kwa inu: cha kuwona masomphenya.

Ndi anthu angati mkati muno anayamba alotapo loto. Tiyeni tiwone dzanja lanu. Bwanji, ine ndikuganiza awiri pa atatu a inu. Ndi zoono kuti anthu ena samalota. Ndicho chikumbumtima chanu mutagona, ife timaphunzitsidwa. Apa pali chikumbumtima chanu choyamba; ichi ndi chikumbumtima chanu mutagona. Tsopano, chikumbumtima ichi mutagona ndi chimene ine ndikuyesera, ndi Mzimu Woyera, kugwirirapo ntchito.

Chikumbumtima choyamba ichi. Ine ndikhoza kumufunsa munthu uyu apa, kapena munthu aliyense pano, winawake, “Kodi inu mukukhulupirira?” “O, inde, bwana!” Inu mukukhulupirira izo apa, koma bwanji munthu uyu pansa apa? Iye ndi amene akuyendetsa ngalawa, osati munthu yemwe ali mu nyumba ya woongolera. Ndi munthu yemwe ali mu chipinda cha injini.

Nthawizina pamene iwe upita kuti ukagone, iwe umapita mu chikumbumtima ichi ndipo iwe umalota, ndipo umalota zinthu zimene iwe unazichita pamene iwe unali kuno. Ndiye, pamene iwe udzuka, iwe umakumbukira zinthu zomwe iwe unazilota. Inu anthu amene mwalotapo maloto. Zaka zambiri zapitazo inu munawalota iwo. Inu mukadali kuwakumbukirabe iwo. Chabwino, linalipo gawo linalake la inu kwinakwake (kodi sikulondola kumeneko?), kapena inu sibwezi mukukumbukira izo, chinachake chimene inu munalota zaka zambiri zapitazo.

Tsopano, munthu amene amagona mwankonono, chikumbumtima chake chiri mmbuyo kutali. Icho sichimafika konse kwa iye.

Koma, mpenyi, chikumbumtima chake sichiri kumbuyo uko, ngakhalenso kuti icho chiri pano. Icho chiri pomwe apa. Iye samapita kokagona. Iye ali ndi maso ake chitsegulire, ndipo iye amangopenya.

Tsopano, zimenezo, Mulungu anamupatsa munthu ameneyo malo, pamene iye angakhoze kugona mwankonono ndipo nkusamalota. Mulungu anamupatsa munthu njira yoti azilotera maloto. Ine ndikanati, “Ndilotere ine loto.” Inu simukanakhoza kuchita izo.

Chabwino, ndiye, Mulungu amayika mu mpingo, ena, atumwi, aneneri, mphatso za machiritso. Ndi kulondola uko? Iwo onse ndi opangitsa ungwiro mpingo.

Paulo anati, ngati patabwera... “Ngati inu nonse mutayankhula ndi malirime, ndipo wosaphunzira nkubwera mkati, kodi iye sanena kuti ndinu nonse amisala? Koma ngati mmodzi alosera ndi kuwulula zinsinsi za mtima, kodi iwo sagwera pansu ndikuti zoonadi Mulungu ali ndi inu?” Ndi kulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Kodi umenewo ndi Uthenga? [“Ameni.”] Chabwino, kodi ameneyo sanali Yesu Khristu dzulo? [“Ameni.”] Kodi Iye sali lero? [“Ameni.”] Inu mukhoza kumukhulupirira Iye pa kuyankhula ndi malirime; inu mukhoza kumukhulupirira Iye mwa Mzimu Woyera; koma ine ndikumukhulupirira Iye mu muyezo wathunthu womwe Iye ali, Ambuye Yesu yemweyo. Iye sali wakufa. Iye anawuka kwa akufa, ndipo ali pano usikuuno, pano pa nsanja tsopano. Ndipo Iye atatalitsa ndi kutithandiza.

Ine sindinayambe ndakhalapo mu dziko lino kale. Ndipo, mmene ine ndikudziwira, palibe wamoyo amene ine ndikukhoza kumuwona patsogolo pa ine yemwe ine ndikumudziwa, apang’ono kwambiri pano pa nsanja. M’bale Boaz, ine ndikumukumbukira iye. Ine ndinamuwonapo munthu uyo ali pafupi ndi iye; ine sindiri kukumbukira dzina lake. Koma, ndipo ine... M’bale Lindsay. Okhawo mwina atumiki atatu kapena anai akhala pano omwe ine ndikuwadziwa, mu nyumba ino. Koma, Mulungu akukudziwani nonse a inu. Ndi zoono izo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Iye akukudziwani nonse a inu.

Tsopano, dona uyu wayima pano, Mulungu Kumwamba akudziwa kuti ine sindinayambe ndamuwonapo iye mu moyo wanga, monga ine ndikudziwira. Kodi ndife alendo, dona? [Mlongoyo akuti, “Inde, bwana.”—Mkonzi.] Ife ndife alendo mwangwiro. [“Inde.”] Koma Mulungu akumudziwa iye.

Tsopano, ngati Yesu ali yemweyo dzulo, lero ndi nthawizonse, tiyeni tisinthe chithunzi tsopano. Chimene Iye anali dzulo, pamene Iye anali kuti akapeze chinachake cha mkazi, Iye anati, “Ndi bweretsere Ine madzi.”

Iye anati, “Bwanji, si mwambo wake kuti izi zichitike, Ayuda ndi zina zotero, ndi Asamariya.”

Koma, Yesu akuyankhula kwa iye kwa kanthawi, pang’ono, Iye anapeza basi pamene vuto lake linali. Ndi kulondola uko? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.]

Chabwino, tsopano, Yesu wawuka kwa akufa, tsopano, ndipo akukhala mkati mwa ife usikuuno. “Kanthawi pang’ono, dziko silindiwonanso Ine, komabe inu mudzandiwonona Ine, pakuti Ine...” “Ine” ndi puronauni ya umwini. “Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka ku mathero a dziko.” Tsopano, ndicho Choonadi cha Uthenga. Inu mwina munali musanawerengepo Izo mwanjira imeneyo, kapena kuganiza za izo mwanjira imeneyo, koma ndi momwe izo zinalembedwera mu Baibulo. Mwakuti, zamulungu zanu zikhoza kuti zinalambalala Izo kwinkwawe, koma ndi momwe Izo zalembedwera mu Baibulo. “Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka ku malekezero a dziko.”

Tsopano, inu mukudziwa ine ndikuyembekezera chinachake. Izo ndi zoono. Ndi Mngelo wa Ambuye. Ndizo zoono. Ndine wopanda chochita basi monga ine ndikanakhalira, basi monga ena onse a inu. Ndipo ine ndiri pano mwinamwake ndi otsutsa atakhala pano.

Ndi angati anayamba awonapo chithunzi Chake, amadziwapo za misonkhano yanga ndipo anawona kumene asayansi anajambula chithunzi Chake, Kuwala Kwakukulu kumene kumabwera mkati ndipo inu nkukhoza kukuwona Iko? Inde, ambiri a inu. O, zikwi za mapapala a zomwe zagulitsidwa, ndi zina zotero. A Douglas Studio mu Houston Texas ali nacho icho, kumene George J. Lacy, mmodzi wa opambana mu kafukufuku mu Amerika, anachitenga icho ndi kukachipima icho, chirichonse, kuti awone kuti sikunali kujambula kwapawiri kapena chinachake. Ndipo Yesu Khristu anadzitsimikizira Iyeyekha kukhala ali yemweyo dzulo, lero ndi nthawizonse.

Tsopano, ndithudi, ine ndikuyembekezera pa Iye. Kaya Iye andithandiza ine usikuuno, ine sindiri kudziwa. Ndipo ngati ine ndanena chirichonse modzitama, kapena chirichonse chimene ine ndachinena mochoka pa njira, Mulungu atandikhululukira ine. Ine sindikanatanthauza kuti ndichite izo. Ine ndimatanthuza kokha, ndi kudzichepetsa kwa mtima, kuti ndimuyimire Yesu Khristu Yemwe akumvetsera kwa ine tsopano. Ndipo chifundo Chake chitakhala pano usikuuno. Pokhala kuti ine ndayankhula zinthu izi, ndipo ine pokhala mu Mawu Ake, Iye atabwera ndi kudzatithandiza ife, ndilo pemphero langa.

Ndipo, tsopano, kodi walimba ali pano penapake? Ngati iye angathe, mosafulumizitsa, chonde, motsika kwenikweni, nyimbo ya, Kungo khulupirira.

Ndipo aliyense chonde akhale mu—chikhalidwe cha pemphero, ngati inu mungathe. Inu simukusowa kuti muweramitse mutu wanu kupatula ngati inu mutafunsidwa.

Tsopano, mu mzere wa pemphero, inu amene mukubwera, chomwe chingakhale... Ngati Iye akudzudzulani inu, inu muyenera... ngati chiri... Icho chikakhala choona. Ngati icho chiri, inu muyenera kukhala wololera kuyima ndi icho. Mwa omvera, kulikonse, ngati Iye anena, inu muyenera kudziwa kuti si ine. Ndi Iyeyo. Ndipo mupite mukazikonze izo. Chinthu choyamba chimene inu mungakhoze kuchita, inu musanati mupeze kuchiritsa, inu muyenera kupeza choyambitsa inu musanapeze kuchiritsa.

Ngati inu mutapita kwa dotolo, wodwala ndi kutsegula, ndipo iye nakupatsani inu asipirini, iye si dotolo wabwino. Iye akuyesa kukuthamangitsani inu. Ngati iye ali dotolo wabwino, iye angapime vutolo mpaka iye atalipeza vutolo, ndiyeno nkuyamba kugwira ntchito kuchokera pamenepo.

Ndicho chinthu chofanana chimene ife tiyenera kuchichita pano. Ngati mzimu woyipa, ngati pali tchimo losalapidwa, kapena chinachake, kapena china cha kunja kwa chifuniro cha Mulungu; inu mukhoza kuwadzoza iwo, utali wonse wa usiku, ndi kulira ndi kufuula, ndi kuchita zonse zimene inu mukukhumba kuchita, chiwanda chimenecho chikhala apo pomwe. Ndiko kulondola. Iye ali nawo ufulu wotero. Koma ndicho chimene inu muyenera kuchisamalira; Mulungu akayika themberero pa winawake chifukwa cha chinachake, ndiye iwe nkubwerapo kuti udzalichotsepo ilo, iwe ulowa mu vuto monga Mose anachitira. Ndiko kulondola.

Iye ali pano, Mzimu Woyera. Tsopano, mu dzina la Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, ine ndikumutenga munthu aliyense mkati muno pansu pa ulamuliro wanga, kwa ulemerero wa Mulungu.

Tsopano ine ndikufuna kuti ndiyankhule nanu miniti, mlongo. Inu mukukhudzidwa kuti chinachake chikuchitika, ndithudi. Mwaona, mwaona, icho chachitika kumene tsopano. Tsopano, ngati izo ziri zoono, aloleni anthu awone, ndi dzanja lanu lokwezedwa. Ndiko kulondola. Mwaona? Ndi zimenezo. Ndiko kukhalapo Kwake. Ndi kulondola. Mwaona?

Tsopano, ine, ndine mlendo kwa inu, ndipo sindinayambe ndakuwonanipo inu mu moyo wanga. Ndipo tsopano ngati Mzimu Woyera, umene ine ndimawukamba, wa Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero ndi nthawizonse; ngati ine ndachitira umboni izo moona kwa anthu, ndi kulengeza izo kuti ziri zoono, ndipo Iye ali yemweyo, ndiye Iye awulula kwa ine chinachake, kwa inu, chimene chiti chikuthandizeni inu kuti mumukhulupirire Iye. Ngati inu muli pano... Ine sindikudziwa chimene inu muli kuchisowa, kaya ndi... koma Iye akudziwa. Tsopano, ngati Mulungu ati aloleze izo, kodi inu muvomereza machiritso anu ndi... kapena—kapena chirichonse chimene chiripo inu mukuchifuna, ndalama, kapena chirichonse chimene

chiri chomwe inu mukumufunira Iye, kapena kuti mumufunse Iye pa icho. Kapena, mavuto apa khomo, chirichonse chimene chingakhoze kukhala, chirichonse chimene icho chiri, Iye achidziwa, ndipo Iye akhoza kundidziwitsa ine. Ndi kulondola kumeneko? [Mlongo akuti, “Kulondola.”—Mkonzi.] Ndipo izo zikanati zimupange Iye yemweyo monga Iye ankayankhula kwa mkazi pa chitsime. [“Inde.”]

Tsopano ine ndikungoyankhula kwa inu, monga Iye ankachitira, kuti ndikhudze mzimu wanu. Ndipo ine ndikuwona inu mukusuntha kuchoka kwa ine. Ndinu—ndinu. . . Inu munali ndi. . . Ine ndikuwona kugundana kwakukulu kwa mtundu wina. [Mlongo akuti, “Inde.”—Mkonzi.] Ndi ngozi. [“Inde. Inde. Inde.”] Ndipo inu. . . Iko kunali kugundana kwa galimoto. [“Inde.”] Ndipo inu munaponyedwera mu mlengalenga, monga choncho. [“Inde.”] Ndipo izo zinakunyokani inu, penapake pa khosi lanu, izo zayambitsa—khansara kuti abwere mu khosi lanu. [“Inde.”] O, ndipo muli ngati wophunzitsa winawake, mu Lemba. Ndipo kodi inu mukukhulupirira kuti Yesu Khristu akuchizani inu? [“Ine ndikutero.”]

Atate, Mulungu, mu Dzina la Mwana Wanu, Yesu Khristu, pa ulamuliro wa Mawu a Mulungu, kwa mkazi amene akufa, ine ndikupempha kuti chinthu choyipa ichi chimusiye iye.

Satana, iwe wayalusidwa, chotero tuluka kuchokera mwa mkaziyu, pamene Mpingo wa Mulungu wamoyo ukukuyitana iwe kuti uchoke, mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

[Mlongo akuti, “Zikomo inu. Zikomo inu. Zikomo inu.”—Mkonzi.]

Tsopano, mlongo, mphindi yokha; ndikungofuna kuti ndiyankhule kwa inu. Ndithudi, inu mukudziwa kuti icho chachoka tsopano. [“O, inde.”] Iko kukhala mwanjira imeneyo. Mukuona momwe kummero kwanu, kwafewera? Ndipo. . . [“O, inde. Ambuye alemekezeke.”] Izo zonse zachoka kwa iye. Cho—chotupa chachoka pa mmero pake. Ndipo iye. . . Mulungu akudalitseni inu. Pitani pa msewu wanu tsopano, ndipo mukakhale othokoza kwambiri, ndi wokondwa ndi kusangalala. Ndipo—ndipo mukakhala. . .

Tsopano, khalani nacho chikhulupiro basi mwa Ambuye Yesu. Mpangeni Iye, wanu. . . chirikati cha lingaliro lanu pakali pano, Ambuye Yesu, pamene inu mukulingalira pa zinthu izi. “Pamene iwo anali akulingalira pa zinthu izi, iwo anali mu umodzi wachiyanjano. Kumbukirani, “Yesu yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse.” Iye ali yemweyo lero.

Tsopano khalani ndi chikhulupiro. Penyani mbali ino, omvera, ndipo khulupirirani ndi mtima wanu wonse. Ndipo mundipatse ine chidwi chanu chosagawanika. Khalani mu pemphero. Sungani chikhulupiro mwa Mulungu.

Tsopano, ine ndikukhulupirira donayo ndi uyu. Kodi uyu ndi wodwala? [M'bale akuti, "Inde."—Mkonzi.] Chabwino. Bwerani pafupi, mlongo. Ndithudi, Icho sichikupwetekani inu tsopano. Uko, Ndiko Kukhalapo Kwake basi, mwaona, kumene inu mukukumverera. Ndipo ine . . .

Ndipo, omvetsera, ine—ndine m'bale wanu. Ine . . . Uku si kuwerenga maganizo, ine ndachimverera icho chikubwera kuchokera kwa omvera. Si izo. Ndi Mulungu Wamphamvuzonse. Mwaona? Mwaona? Si kuwerenga maganizo ayi. Ayi, sindizo. Tsopano, musati muzichita zimenezo. Zingoganizani kuti ndi Ambuye Yesu, onani, mwa umodzi wachiyanjano.

Tsopano, mlongo, ine ndikungofuna kuti ndiyankhule ndi inu mphindi yokha. Ndife alendo, ine ndikuganiza. Koma, Yesu Khristu akutidziwa tonse a ife. Ndipo iyi ndi nthawi yathu yoyamba kukomana pa dziko lapansi. Koma Iye akukudziwani inu, ndipo Iye wakudyetsani inu moyo wanu wonse. Ndipo Iye amandidziwa ine. Ndipo ngati ine, m'bale wanu, ndipo mwa chisomo Chake, mwa mphatso Yauzimu . . . kuti ine ndinalibe kanthu koti ndichite pa kubwera kwa iyo. Pamene ine ndinabadwa, mwana wamng'ono, chinthu choyamba chimene ine ndingakhoze kuchikumbukira chinali masomphenya.

Tsopano, ine ndikufuna inu muyang'ane mbali iyi mphindi yokha. Ndithudi, ndinu wodwala. Ndipo inu mukuvutika ndi—chikhalidwe chomwe chiri . . . Ndi mzimu wakuda pozungulira inu. Ndi imfa. Ndipo iyo ili mu mawonekedwe a khansara. Ndipo khansarayo ikupezeka pa bere. Ndipo ndinu . . . Ine ndikukuwonani inu mukupimidwa ndi winawake wamphamvu. Ndipo ndi . . . inu muli ndi—chikhalidwe cha wachotupa. Ndipo chotupacho chiri mu matumbo. Ndipo inu muli ndi vuto la mmimba, naponso. Vuto lopweteka la mtima limene limakupangitsani inu kukomoka. Kuno masiku angapo apitawo, inu munali mutakhala chammbali pa mbali ya kama, ndipo pafupi kukomoka, mukuyang'ana cha ku zenera.

Kodi zinthu zimenezo ndi zoona? [Mlongo akuti, "Inde, bwana, zonse zoona."—Mkonzi.] Izo zinali zonse mooni. Chabwino, chirichonse chimene icho chinali, chifukwa, izo zachoka kwa ine.

Koma inu mukuganiza kuti icho chinali chiyani chimene chikudziwa moyo wanu? Kodi uyo anali Yesu Khristu? Inu mukuvomereza icho kuti ndi chimenecho? [Mlongo akuti, "Inde."—Mkonzi.] Zikomo inu. ["Ndipo ine ndikukhulupirira ine . . ."] Inu mukulolera . . . Inu mukudziwa kuti chinachake chazimu chiri pano. ["Inde."] Ndipo ngati inu mukukhulupirira Icho kuti chiri Ambuye Yesu, monga ine ndalalikirira izo kuchokera mu Mawu! Ndipo inu mukukhulupirira icho kuti chiri Ambuye Yesu? ["Inde. Ine ndikutero."]

Ine ndikudziwa kuti pali mzimu wakuda. Ine ndikuwuwona iwo utapachikika pa inu panobe. Ndi chinachake chowopysa kwambiri. Inu mukuti. . . Ine ndikukuwonani inu. Dzina lanu ndi Eva. [Mlongoyo ati, “Inde.”—Mkonzi.] Ndipo dzina lanu lotsiriza ndi York. [“Inde.”] Ndipo inu mumakhala mu mzinda uno. [“Inde. Ine ndimakhaladi.”] Ndipo nambala ya nyumba yanu ndi 613 Msewu wa Chisanu ndi chimodzi. [“Inde.”] Ndi kulondola uko. [“Inde.”] Inu mupita kwanu, kukakhala bwino.

Mu Dzina la Yesu Khristu, muloleni iye apite ndi kukakhala bwino.

Mulungu akudalitseni inu. Pitani, mukusangalala ndi wokondwa mukukhulupirira pa Ambuye Yesu Khristu.

Ingokhalani ndi chikhulupiriro. Musati mukayikire. Lemba lanena kuti, “Pitani inu ndipo musati mukachimweso, kuwopa kuti chinthu choyipisitsa chingabwere pa inu.” Tchimo ndilo kusakhulupirira. Tchimo si kumwa, kusuta, njuga; ndizo zotsatira za tchimo. Inu mumachita izo chifukwa inu simumakhulupirira ayi. Yesu anati, “Pita ndipo usati ukachimweso (kapena, “kusakhulupirira” kenanso ayi), kapena zinthu zoyipisitsa zikabwera pa iwe.” Khalani nacho chikhulupiriro mwa Mulungu. Mumukhulupirire Iye ndi mtima wanu wonse.

Ine ndikuwona Kuwala kukumutsatira mkazi uyo, panobe, Iko kwangokhala. . . ngati ali iye yemwe wangochokayu. Iko kuli kupachikika pa munthu wachikuda apo. Inde, donayo apo, yemwe ali ndi ndulu ndi chotupa. Kodi inu mukukhulupirira Ambuye Yesu angakuchizeni inu, dona wakhala apoyo ali ndi chinthu choyera mozungulira khosi lake? Ngati inu mukukhulupirira izo, ndi mtima wanu wonse, inu mukhoza kuwuka ndi kutenga machiritso anu, ndipo muchiritsidwe mu Dzina la Ambuye Yesu. Mulungu akudalitseni inu.

Khalani nacho chikhulupiriro mwa Mulungu. Kodi inu mukukhulupirira?

Inu muli ndi chotupa, si choncho inu, bwana, mwakhala pamenepo uko? Kodi si kulondola kumeneko? Inu munali mutakhala pamenepo, mukupemphera, “Ambuye, mchititseni munthu ameneyo kuyankhula kwa ine.” Ndi kulondola uko? Ngati kuli kulondola, kwezani dzanja lanu. Imirirani pa mapazi anu. Chikhulupiriro chanu chakuchizani inu, m’bale. Pitani kunyumba; Yesu Khristu wakuchizani inu.

Ambuye Yesu yemweyo! Inu simukusowa kuti mukhale pamwamba pano. Inu mukusowa kukhala nacho chikhulupiriro. Ingo khulupirirani Mulungu, ndi mtima wanu wonse, ndipo inu mukhala nazo zimene inu mukupempha. Yesu Khristu apereka izo kwa inu ngati inu muti mungokhulupirira. Koma inu muyenera kukhala nacho chikhulupiriro. Inu muyenera

kumukhulupirira Iye, ndi mtima wanu wonse, ndipo Mulungu azikwaniritsa izo.

Wodwala. Ndikhululukireni ine, bwana. Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Inu mukutero? [M'bale akuti, "Inde."—Mkonzi.] Tsopano inu mwatengeka chabe pang'ono chifukwa cha Kukhalapo kwa Umunthu Wake utayima pano. Ndipo ine ndikukhulupirira ndinu wochokera kunja kwa mzinda. ["Inde, bwana."] Inu mukuchokera ku likulu, inunso. Richmond. ["Eya."] Virginia. Inu muli ndi khansara. Iyo ili mwa inu...mkati mwa kamwa yanu, pa nsagwada yanu. Ndi kulondola kumeneko? Inu mukufuna kupita kwanu ndi kukachira? ["Inde, ine ndikufuna."] Mulandireni Yesu ngati mchiritsi wanu. ["Inde, bwana."]

Ndipo mu Dzina la Yesu Khristu, chitamusiya bamboyu, chichoke kwa iye. Amen.

Mulungu akudalitseni inu bwana. Pitani, mukukhulupirira, muli ndi chikhulupiriro, ndi zonse...

Kodi inu mukuti chiyani? [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Ine ndikudziwa tsopano, kuti pokuwonani inu, inu mukusanduka munthu wowoneka-wamng'ono, wamng'ono kwambiri kuposa chimene inu muli pamaso panga. Inu mukuvutika ndi mtundu wina wa mutu. [Mlongo akuti, "Ndiko kulondola, mutu."—Mkonzi.] Ndipo iwo—iwo wabwera zaka zambiri zapita, pafupi zaka makumi awiri ndi zisanu zapitazo, mutu wanu unayamba. ["Ndiko kulondola."] Ndipo iwo wakhala ukukuvutitsani inu chiyambireni. Inu mwakhala muli wokhulupirira kwambiri. Ndipo inu—inun munapempherera ora ili limene mwayima pano tsopano. Inu munanena mu pemphero, kwa Mulungu, kuti ngati inu mukanakhoza kokha kufika kwa ine, kuti ngati ine ndikadapemphera, mwakuti mutu wanu ukanasiya. Zinthu zimenezo ndi zoono? ["Chirichonse."] Izo ndi zoono.

Tsopano, inu mwamva Chimene chimanena izo. Ameneyo sanali ine; ilo linali liwu langa chabe. Zinali izo chirichonse chomwe chinali, chinali chinachake... ine—ine ndikukumbukira kumuwona munthu wamng'ono kapena chinachake. Kodi izo zinali basi momwe izo zinanenedwera pamenepo? [Mlongo akuti, "Basi momwe inu mwanenera."—Mkonzi.] Eya, basi momwe izo zinanenedwera. Tsopano, inu mukukhulupirira kuti Mulungu anachita izo? Inu mukumukhulupirira Mulungu...["Ine ndikukhulupirira kuti Mulungu anachita izo. Ine ndikutsimikiza za zimenezo."] Tsopano, inu mukutsimikiza kuti Mulungu ali pano.

Mphindi chabe, ine ndikuwona chinachakenso. Mayi wamng'ono zikuwoneka kuti akuyima pafupi ndi inu. Ndi—ndi mwana wanu wamkazi. Ndipo, inde, inu munali kukonzekera kuti mupite pa ulendo kwinakwake. Inu mumapita kuti

mukamuwone iye. Ndipo iye ali wochokera ku Indiana. Richmond, Indiana ndi kumene iye amakhala. Ndipo iye... Mwamuna wake ndi mtumiki. Ndipo iye wakulemberani inu kalata, chinachake, kukuuzani inu kuti musabwere chifukwa ine ndinali kubwera kuno. [Mlongoyo akuti, “Ndiko kulondola.”—Mkonzi.] Ndi kulondola uko? [“Inde.”] Inu mwachiritsidwa. Inu mukhoza kupita pa ulendo wanu, ndi kukachira. Mulungu akudalitseni inu, mlongo.

Tsopano, kungo khulupirira. Khalani nacho chikhulupiriro mwa Mulungu. “Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse.” Ndipo tsopano ingokhalani nacho chikhulupiriro, ndi kukhulupirira.

Mulungu akudalitseni inu anthu okonedwa achikuda mukufuula. Iye ali—Iye ali nthawizonse wokonzeka kuti athandize, ndi kukhulupirira, kuti awathandize anthu amene akusowa.

Mphindi chabe. Dona... Tsopano ine ndikuwona Mzimu Woyera utayima mu ngodya. Iwo uli pa dona wachikuda. Iye akuyang’ana mbali ino; iye wakhala ali. Ndipo iye akupemphera. Iye ali ndi chophuka, ndipo chophuka chimenecho chiri pa mmero wake. Iye wakweza dzanja lake mmwamba. Inu mukuvomereza machiritso anu, dona?

Dona yemwe wakhala kumbuyo kumene kwa inu pamenepo, nayenso. Iye ali nacho chophuka, ndipo icho chiri pa phewa lake. Ndi kulondola uko, dona? Nonse a inu imirirani pa mapazi anu, pakali pano. Madona awiriwo apo pomwe, ali ndi chophuka pa... Madona awiri achikuda. Yesu Khristu akuchizani inu nonse. Inu mukhoza kupita kwanu ndi kukachira, kwa ulemerero wa Mulungu. Chikhulupiriro chanu chakuchizani inu. Mulungu akudalitseni inu. Ichochachoka.

Khalani nacho chikhulupiriro mwa Mulungu. Musati mukayikire, koma khulupirirani kuti zinthu zonse ziri zotheka kwa iwo amene amakhulupirira. Amenii.

Mai! Ndi kudzaza kotani kwa chikhulupiriro mnyumba muno! Ichochikuwoneka—chikuwoneka mwamkaka kwenikweni, apo pamwamba pa nyumbayi. Inu muli ndithudi mu Mzimu wa Ambuye tsopano. Chirichonse chikhoza kuchitika.

Inu muli bwanji, dona? Kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri wa Mulungu, Wake... ine ndikutanthauza, chabwino, mneneri ndi mlaliki. Inu simukuyembekeza ine kuti ndiri wa mdani; inu mukuyembekeza ine kuti ndiri wa Mulungu. Kodi ndi momwe inu mukulandirira izo? Chabwino, ndiye, ine ndikhoza kukuthandizani inu. Chifukwa, Iye anandiuza ine, ngati ine nditati ndiwafikitse anthu poti andikhulupirire ine, ndi kukhala woonamtima pamene ine ndipemphera, kuti palibe chomwe chikanati chidzayime patsogolo pa mapemphero.

Ndipo, tsopano, si ine amene ndimathandiza. Ndi Mulungu yemwe amachita kuchiritsako.

Ine ndinafunsa, ine ndinati, “Iwo sakandikhulupirira ine.”

Iye anati, “Pakakhala pali zizindikiro ziwiri zitaperekedwa kwa iwe, monga zinali kwa mneneri Mose. Mwa izi, anthu adzakhulupirira.” Ndipo chimodzi cha izo, chinali kuti ndiziwulula zinsinsi za mitima ya anthu, kwa iwo.

Tsopano, inu simuli pano mwanokha. Ngakhale, inu muli wamanjenje ndi wotheratu, koma izo zayambitsidwa ndi matenda a mwana uyu. Mwana uyu pano akuvutika. Iye wakanidwa ndi madotolo, kuti afe. Ndi Leukemia. [Mlongo akuti, “Inde.”—Mkonzi.] Kodi si kulondola uko? [“Ndiko kulondola.”] Inu mwamubweretsa mwanayu kuchokera kunja kwa mzinda. Inu mwayenda, kubwera kuchokera kumadzulo, kubwera kummawa, inu mwabwera. Inu mwabwera kuchokera ku chi—chigawo chomwe chiri ndi mapiri. Ndi Pennsylvania. [“Ndiko kulondola.”] Ndipo mzinda wanu, ine ndikukhulupirira, ndiwo Chambersburg. [“Inde.”] Ndi—si kulondola kumeneko? [“Ndiko kulondola.”] Mbweretseni mwanayo kwa ine.

Mlongo wamng’ono, wokonedwa; Ambuye Yesu akanakhala pano, Iwo bwezi atasanjika manja Awo pa iwe, ndipo imfa ikanakusiya iwe, ndipo iwe ukanakhala moyo. Kodi iwe ukukhulupirira kuti ndine wantchito Wake?

Ndiye, mu malo Ake, ine ndikusanjika manja anga pa mwana uyu ndi kumudalitsa iye, ndipo ndikupempha kuti chiwanda chimusiye mwanayu, ndipo moyo umenewo ubwere kwa mwanayo ndipo iye akhala moyo ndi kukhala bwino. Tuluka mwa mwanayu, Satana. Mwa ulamuliro wa Baibulo la Mulungu, ndi mphatso Yauzimu yotumikiridwa ndi Mngelo, ine ndikukulumulira iwe kuti umusiye mwanayo. Tuluka mwa iye. Amenii.

Iwe ukukhulupirira kuti ukhala bwino tsopano, si choncho, mlongo? Mulungu akudalitse iwe. Tembenukira uku ugwedezere dzanja kwa omvera. Tsopano. Mulungu akudalitseni inu. Msungwana wamng’ono, wa chikhulupiriro chopambana, khala bwino. Mulungu akudalitse iwe, wokonedwa. Pita, ndipo iwe ukandilembere ine kalata.

[Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

Kodi inu mukundikhulupirira ine monga mneneri Wake, monga wantchito Wake? [Mlongo akuti, “Inde.”—Mkonzi.] Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu ali pafupi, ndipo Mzimu Wake, ndi ichi chimene chikuchitidwa tsopano ndi cha Ambuye Yesu? [“Inde.”] Osati ine, ndine munthu. Eya. Ngati Mulungu ati andilore ine kudziwa chimene chiri cholakwika ndi inu, ngati chitsimikizo ine ndine mneneri Wake nditayima pano kumawulula Choonadi!

Monga Iye ananena kwa mkazi, “Pita ukamutenge mwamuna wako.”

Iye anati, “Ine ndiribe aliyense.”

Iye anati, “Iwe wakhala nawo asanu.”

Iye anati, “Ine ndikuwona kuti ndinu mneneri.” Mwaona? “Ine ndazindikira kuti Ndinu mneneri.”

Tsopano, Mzimu womwewo umene unali pa Mwana wa Mulungu ameneyo, Iye analonjeza kuti adzawutumizanso Iwo mwa mawonekedwe a Mzimu Woyera, womwe ukanati udzakhale ndi ife ndi kumakhala mwa ife, mpaka ku mathero a dziko. Inu mukukhulupirira zimenezo? [Mlongo akuti, “Inde.”—Mkonzi.] Ndipo Iye akhoza kudziwa mavuto anu tsopano, angakhoze Iye? [“Inde.”] Inu muli ndi vuto la mtima. [“Inde.”] Kodi ndi kulondola kumeneko?

Munthu aliyense yemwe ali ndi vuto la mtima, imirirani pa mapazi anu. Inu mukhoza kuchiritsidwa pakali pano, ziribe kanthu chimene chiri, ali ndi vuto la mtima.

Ambuye Mulungu, Inu mukudziwa mphamvu zathu ndi momwe ife tiriri ofooka, ndi momwe tiri opanda mphamvu. Ndipo, koma, Ambuye, ife tikudziwa momwe Inu muliri wamphamvu. Ndipo vuto la mtima ndi chinachake chimene madotolo athu sangakhoze kuchitapo chirichonse. Koma, Ambuye, Ndani anapanga mtima? Inu munapanga. Ndipo ine tsopano ndikudzudzula mphamvu ya chiwanda iyi yomwe ikuwagwira anthu awa ndi vuto la mtima. Mulole atuluke iye kuchokera mwa mmodzi aliyense wa iwo, mu Dzina la Yesu Khristu. Amenii.

Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Ine ndikungofuna kuti ndinene chinachake kwa inu. Inu mukumverera mosiyana tsopano kuposa momwe inu mumamverera kwa nthawi yaitali, mukutero inu? [Mlongo akuti, “Inde, ndiko kulondola.”—Mkonzi.] Tsopano, chotero kuti anthu adziwe, pali mzimu wakuda kwenikweni; inu munali ndi kuvutika koyipa, ndi kugona pansu, apo. [“Ndiko kulondola.”] Ndipo tsopano iko kwachoka pa inu. [“Inde.”] Inu mwachiritsidwa. Inu mungopita mukumakanena kuti muli bwino. [“Zikomo Ambuye.”]

Khalani nacho chikhulupiriro mwa Mulungu, chonde. Aliyense, ndi umodzi wachiyanjano, khalani nacho chikhulupiriro.

Inu muli bwanji, bwana? Chabwino. Ife pokhala alendo, wina kwa mzake, koma Ambuye Yesu akutidziwa ife tonse. Kodi ndi kulondola uko? Mulungu Wakumwamba, Yemwe analenga kumwamba ndi dziko lapansi, anadzakhala mwa Yesu Khristu, analonjeza kuti adzabwereranso mwa ife, ndipo chimene Iye anachita ife tidzachichita nafenso. Kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri Wake?


Chifukwa chimene ine ndikunenera izo, Mngelo wa Ambuye anandiuza ine, “Uziwafikitsa anthu poti akukhulupirire iwe. Ndipo ngati iwo sati akukhulupirire iwe, ndiye iwe uzidzadziwa zinsinsi za mu mtima zomwe, ndipo iwo adzayenera kuti akhulupirire izo ndiye.”

Koma, inu muli kundikhulupirira ine. Ndipo pambali pa, chifukwa chimene inu mukundikhulupirira ine, inu ndinu mtumiki wa Uthenga inumwini. Ndipo inu muli pano pa chifukwa chabwino. Inu simuli kudwala. Inu muli ndi chosowa, ndipo inu mukufuna chitsitsimutso cha kachitidwe-kachikale kuti chifalikire kumene inu mukukhala. Ndicho chimene inu mukupempherera.

Aliyense wa ife akufuna zimenezo. Tiyeni tonse tiyime, kufuna chitsitsimutso cha kachitidwe-kachikale.

Mulungu wamphamvuzonse, yemwe munalenga kumwamba ndi dziko lapansi, ine ndikupempha tsopano kuti mphamvu iliyonse ya chiwanda mnyumba muno isweke, Mphamvu ya Yesu Khristu ikhale itawonetseredwa. Ambuye! Ofooka, koma si ndife ogonjetsedwa.

Satana, ine ndikukulamulira iwe, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu, tuluka mwa anthuwo!

Imirirani, inu anthu olumala, kuchokera mu zikuku. Mpatсени Iye matamando, mmodzi aliyense wa inu! 

CHAKUYA CHIMAYITANIRA KU CHAKUYA CHA54-0624
(The Deep Calleth To The Deep)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikiidwa mu Chingelezi pa Lachinayi usiku, Juni 24, 1954, ku Constitution Hall mu Washington, D.C., U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 1997 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©1997 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org